JW.ORG™
Koperani nkhaniyi pa www.jw.org

Zokuthandizani Kuyankha Mafunso

Kodi mumamva bwanji munthu wina akakufunsani zimene mumakhulupirira ku chipembedzo chanu? Ambiri amachita mantha, ndipo zimenezi n'zachibadwa. Tawerengani lemba la Yeremiya 1:6-8, kuti muone zimene Yeremiya ananena ndiponso mmene Yehova anamulimbikitsira. Yehova anathandiza Yeremiya, ndipo inunso adzakuthandizani kuti muzilimba mtima n'kuuza ena zimene mumakhulupirira.

Chinanso chimene chingakuthandizeni kuti mulimbe mtima, n'kukonzekera. Monga banja, onani mafunso osiyanasiyana amene ali pa jw.org pagawo lakuti "Mafunso Okhudza Mboni za Yehova Amene Anthu Amafunsa Kawirikawiri." (Pitani pamene alemba kuti ZOKHUDZA IFEYO > MAFUNSO OFUNSIDWA KAWIRIKAWIRI.) Sankhani funso limene mukuona kuti munthu wina akhoza kukufunsani, ndipo werengani yankho lake. Aliyense wa inu afotokoze mmene angayankhire funsolo m'mawu akeake. Kenako bwerezaninso kuyankha funsoli aliyense payekhapayekha mosinthana. M'malo mofunikira kulembamo mawu olankhulidwamo, omwe ali pamwamba pa mwanayo, lembanimo funso limene mungafunsidwe. M'malo enawo, lembanimo zimene mungayankhe.



▶ **TAYESANI IZI:** Dziwani zambiri zokhudza mneneri Yeremiya. Koperani Khadi la Munthu Wotchulidwa M'Baibulo, lonena za Yeremiya, pa jw.org. (Pitani pa ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA > ANA > KHADI LA MUNTHU WOTCHULIDWA M'BAIBULO.) Yankhani mafunso amene ali pakhadipo, ndipo kenako werengani khadilo kuti muone ngati mayankho amene mwalembawo ndi olondola.

www.jw.org © 2013 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania